Imfa ndi kuuka kwa Ambuye Yesu



Mogwirizana ndi Uthenga wa Mulungu:
Luka 23:33-46, 24:1-10

Cilankhulidwe: CiNyanja



Usiku wa lacinai, anamtengera Yesu kundende. Anamuweruza mpaka ku imfa.

Lacisanu kummawa asirikali anamtengera Yesu kumalo a “Caveira”. Komweko anampacika Yesu pamtanda.

Anamkhomera pamtanda. Panali acifwamba awiri pamodzi ndi Yesu.

Yesu anati: —Atate akhululukireni anthu awa. Musakumbukire coipa cao. Iwo sakudziwa coipa cimene akucita.

Asirikali anagawana mwa iwo zobvala za Yesu. Anacita maere.

Wakulu wa anthu a ku Israeli aseka Yesu. Iwo anati: —Iye anaciritsa anthu ena. Dziciritse iwe wekha.

Panali cikwangwani pamtanda pa mutu wace. Cikwangwani cinati: —Uyu ndiye Mfumu ya Ayuda.

Mwa mmodzi wa cifwamba anacitira Yesu mwano. Iye anati: —Iwe sindiwe munthu amene Mulungu anakakutumiza. Sindiwe ayi! Dzipulumutse iwe wekha. Upulumutse ndi ife tomwe.

Winayo anati: —Leka kulankhula iwe. Akuzunzika monga iwenso. Ife tikunzunzika cifukwa ca coipa tinacita. Koma iye sanacite coipa ciriconse.

Uyu anati: —Yesu, mundikumbukire ine. Mukalowa mu Ufumu wakumwamba.

Yesu anamuuza: —Lero lomwelino ukhala ndi ine mum'Paradaiso.

Inali frikoloko ya madzulo. Yesu anafuula mokweza: —Atate, ndipereka mzimu wanga mmanja mwanu!

Pakunena izi iye anafa.

Anaika mtembo wa Yesu mmanda. Osemedwa pa mwala. Anabvundikira citseko ca manda ndi mwala waukulu.

Linadutsa la cisanu. Linadutsanso loweruka.

Ndipo kunaca la Mulungu. Azimai anapita ku manda. Iwo anatenga mafuta. Kupita nawo kumanda.

Anafika pakhomo la manda. Wina wace anacotsa mwala wa pakhomo. Thupi la Yesu sirinali m'mandamo.

Azimai sanadziwa cokumbuka. Amuna awiri anafika pafupi ndi iwo.
Amuna awiriwo anabvala zobvala zowala.

Iwo anakhala ndi mantha. Iwo anagwada. Anthuwo anati: —Cifukwa ciani inu mufuna Yesu pakati pa akufa. Iye ali ndi moyo. Iye sali muno. Koma iye wauka. Onani, kumbukirani, iye ananena kwa inu: “Ine ndifuna kufa

cifukwa ca ocimwa." Iye anafuna kuti iwo akampacike. Mulungu amafuna akamuukitse.

Azimai anakumbukira za mau a iye. Iwo analongosola zonse kwa wophunzira khumi ndi m'modzi ndi enanso. Onse anakhala wodabwa.

Sankhani mafunso owona:

- Yesu anaphedwa pakati pa anthu awiri acifwamba.
- Mkulu wa asirikali anatenga zobvala za Yesu ndipo anakana kugawana ndi ena.
- Mwa mmodzi wocita zoipa anamcitira mwano.
- Ndipo winayo analankhula mosiana ndi mmene winayo anayankhulira.
- Mulungu anapereka moyo kwa Yesu (anauka) tsiku la citatu.

Mafunso:

1) Manda nciani?
2) Citanthauza ciani kuuka?
3) Mcifukwa ciani anadabwitsika?

Ficha Técnica:

Título: Imfa ndi kuuka kwa Ambuye Yesu
(A Morte e a Ressurreição do Senhor Jesus)
(The Death and Resurrection of Jesus Christ)

Língua: Cinyanja

Artista: Mbanji Bawe Ernest

Primeira edição electrónica, 2010

Produzido por: Wycliffe SA
lidemo.net@gmail.com
C.P. 652
Nampula, Nampula
Moçambique

O utilizador pode copiar e distribuir a obra